

Kusunga chilankhulo cha pa banja lanu kumapanga maziko a kukula kwa chilankhulo chonse m'tsogolo. Mwana wanu akhoza kutenga zilankhulo zambiri pomwe danga lapezeka la kuona, kumva ndiponso kulumikizana ndi njira zina zolimba za chilankhulo.

Antchito Wosamalira Ana a Chichepere mu Victoria amatsogozedwa ndi chigawo cha *Victorian Early Years Learning and Development Framework* (VEYLDF). Dongosololi limazindikira kuti kulankhula zilankhulo zambiri ndi chinthu chabwino ndipo lidakhazikitsa zoyembekezeka zakuti ana adzathandizidwa kusunga chilankhulo kapena zilankhulo za banja lawo, kuphunzira Chingerezi ngati chilankhulo chongoonjezera ndi kuphunziranso zilankhulo zina pomwe akuchita maphunziro awo a ana a chichepere ndi kulandira chisamaliro, Early Years Education and Care programs (VEYLDF, 2016).

Pali phindu lalikulu la mwana wanu kulankhula ndi kusunga chilankhulo kapena zilankhulo za pa banja:

- Mwana wanu atha kuonjezera pakukhala ndi maganizo omvetsa pomwe akugwiritsanso ntchito chilankhulo cha pa banja.
- Kusunga chilankhulo kapena zilankhulo za pa banja ndikofunikira pakupititsa patsogolo ubale, pakupanga kulumikizana komanso kudziwa mbali imene uli.
- Chilankhulo kapena zilankhulo za pa banja zimalumikizana kwambiri ndi zodziwitsa mwana wanuyo, chikhalidwe ndi kukhala bwino kwake.
- Kulankhula bwino chilankhulo kapena zilankhulo za pa banja kumathandiza mwana wanu kuphunzira zilankhulo zoonjezera monga Chingerezi.

A VEYLDF (2016) imafotokoza aphunzitsi kuti 'kukhala ndi kusunga kwa chilankhulo choyamba kapena zilankhulo za pakhomo ndi chaphindu kwambiri ndipo zimathandiza pomanga chizindikiritso cha munthu' (tsamba 18). Mwa ichi, gawo lofunika kwambiri pakuthandiza kukula kwa Chingerezi ngati chilankhulo choonjezera ndi kuti ophunzitsa ndi mabanja azithandizana mwa mgwirizano kulimbikitsa ndi kuthandiza ana kupitirizabe kulankhula ndi kusunga chilankhulo kapena zilankhulo za pa banja lawo.

## Kutukula Chingerezi ngati Chilankhulo Choonjezera mu Maphunziro a Ana a Chichepere ndi Njira za Kusamalira Zowazungulira.

Mwana wanu adzakhala ndi danga la kuphunzira Chingerezi mu Maphunziro a Ana a Chichepere ndi Njira za Kusamalira Zowazungulira mu Victorian. Kafukufuku akutsimikiza kuti 'ana

angathe kuphunzira Chingerezi (kapena chilankhulo china) ngati chilankhulo choonjezera kupyolera mwa kudziwitsidwa chilankhulocho, mwa njira zakuphunzitsira chilankhulo zofotokoza mwatsatanetsatane ndi nthawi yoyenera kulandira chilankhulo chatsopano' (VEYLDF, 2016, tsamba 22).

Kudziwa chilankhulo chimodzi kungathe kuthandiza ana kumvetsa momwe zilankhulo zina zimagwiritsidwira ntchito. Maluso amene ana amapata m'chilankhulo chimodzi akhozanso kugwiritsidwa ntchito m'chilankhulo chatsopano. Ndi kudzera mu chilankhulo cha pa banja kuti ana awa akhoza kuonapo nzeru pa chilankhulo chatsopano, malamulo ake ndi mawu ake. Pamene mwana wanu walowerera kwambiri m'chilankhulo cha Chingerezi, adzakhala ndi danga lakumva Chingerezi munkhani zosiyanasiyana. Adzafuna kuti nayenso alowelerepo pakusewera ndi ana ena ndipo ophunzitsa adzapereka njira zabwino ndi danga loti mwana wanu amve ndi kulankhula Chingerezi mobwerezabwereza.

Maluso a chinenero amakula molingana ndi zomwe mwana adaphunzira kale mchinenerocho, kukumana ndi chinenero chatsopano ndi malo atsopano omwe akuphunzira. Ana amene amaphunzira zilankhulo zambiri pa nthawi imodzi mwina atha, kwa nthawi yochepe, kulankhula chilankhulo chimodzi kwambiri koposa china. Poyamba, ana amatha kusakaniza zilankhulo akamalankhula. Akhoza kudziwa liwu m'chilankhulo chimodzi koma osalidziwa liwulo m'chilankhulo china. Poonetsetsa kuti kukambirana kupitirirabe, iwo amagwiritsa ntchito mawu womwe akuwadziwa kale. Ili ndi luso lachibadwidwe ndi losavuta limene ana amagwiritsa ntchito pomwe akugwiritsa ntchito zilankhulo zawo pa nthawi yazilankhulo zambiri.

## Kumbukirani...

Pamatenga nthawi kuti azitha kulankhula bwino kwambiri mu chilankhulo chatsopano ndipo ana amafuna nthawi komanso thandizo losakakamidwa kuchokera kwa akuluakulu womwe ali pafupi nawo pomwe akuyesetsa kuphunzira chilankhulo choonjezera pa china.

Ndi Ufulu wa ana wonse kuphunzira ndi kugwiritsa ntchito chilankhulo kapena zilankhulo za m'mabanja awo (UNCRC, 1989).

### Maumboni

Department of Education and Training, 2016. *Victorian Early Years Learning and Development Framework*.

UNICEF, 1989. *United Nations Convention on the Rights of the Child* (UNCRC).